MBIRI YA KATEKISIMU YA BAIBULO
MBIRI YA CHIPANGANO CHATSOPANO

Akulu (Kalasi Yachitatu)
Buku La Chiwiri La Awiri

Wolemba ndi **Rev. H. Veldman**
Mkonzi ndi **J.J.Lim**
Wothandizira Wapadera ndi **David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

February 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Katekisimu wa mbiri ya m' Baibulo- Nkhani za mBaibulo za Chipangano Chatsopano
(Ophunzira achikulire- Buku lachiwiri la awiri (2/2))

Lalembedwa ndi **Rev H. Veldman**
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi Rev H.Veldman eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

MAWU A MLEMBI

Buku la katikisimu ili lakhazikika pa ganizo loti Genesis 3: 15 ndi pangano lokhazikika, kulengeza koyamba kwa uthenga wa chipangano ndipo kuti mbiri ya chipangano cha kale ndi kutambasuka kwake m'chipangano chimenechi.

Mogwirizana ndi ganizo cha sinodi ya mpingo wa Protestant Reformed mchaka cha 1955 mpaka 1963,wolemba bukuli wakonza katikisimu wa malangizo mogwirizana ndi achinyamata.

Buku ili lalembedwa kwa ana a pakati pa zaka khumi ndi chimodzi (11) ndi khumi ndi ziwiri (12) ndipo pongounikira langizo la abusa a G.Vanden Berg's muchipangano chatsopano kwa achinyamata. Cholinga cha bukuli sikungowapatsa mfundo zokha za chipangano cha tsopano komanso kuwadziwitsa choonadi chenicheni chomwe mfundozi zikutiphunzitsa ndikukhala ndi chiyembekezo mu mipingo ya yobweleranso ku mau a Mulungu (Protestant Reformed).

Kukamba mwatchutchu mapu ndiwofuka kwambiri kwa ophunzira a kalasi la katekisimu. Izi ndizofunika maka potsata bwino maulendo a Mtumwi Paulo.

Mlembiyu akuthokoza kwambiri anthu onse amene anathandiza polemba bukuli. Tikuthokozanso mwapadera aphunzitsi a pa sukulu yathu ya Adams St. Protestant Reformed Christian School, komiti ya Synod yopanga buku ya Katekisimu, ndi komiti ya Synod yowunika popereka maganizo apamwamba kuti bukuli likhale lophikika bwino.

Ndikupempha kuti Mulungu wathu wa pangano agwiritsenso ntchito bukuli kuti kwa Iye kukhale ulemerero kudzina lake ndi kamangidwe ka pangano la ana athu.

- Rev H Veldman

MAWU A MKONZI

Buku ili (February 2011 edition) linatsindikizidwa kuchokera ku zomwe a PRC a ku America anagwiritsa ntchito zaka makumi anayi zapitazo mowapindulira. Zolakwika zina monga zakalembwe zinachotsedwa ndipo mafunso ena ndi mayankho achepetsedwa ndi cholinga choti akhale osavuta kwa achinyamata kuti athe kukumbukira zonse mopanda kutaya mfundo iliyonse.Verse loloweza pamtima lonse lachokera ku Aroma 8 yomwe yawonjezera ubwino winanso kwa achinyamata.Kuwonjezera kwa mau ena aumboni komwe kunaperekedwa ndi Pastor David Higgs kudzalimbikitsa luso la kupititsa patsogolo maphunziro a ophunzira mosamala ndi chuma chopambana kwa onse ogwiritsa ntchito bukuli pophunzirira.

Mmonga mmene lilili buku loyamba la kalasi iyi ,ophunzira adzapeza kuti mayankho aliko pang'ono ndi mfundo zogwirika ndizozama poyerekeza ndi mayankho a kalasi ya ana. Kuwonjezera apo, kutsindika kwenikweni pa kalasi imeneyi kwambiri ndi kumvetsetsa osati kungowuzidwa mfundo.Choyenera kudziwa makolo ndi aphunzitsi sayenera kutsindika kwenikweni pa mawu pamene akufuna mayankho kuchokera kwa achinyamata.

Ambuye atidalitse tonse ndipo atipatse kupirira pamene tikufuna kuphunzitsa ana athu kuti adzakhale anyamata ndi atsikana a bambo yemwe ali wodzodzedwa ndi uthenga ndi chiphunzitso.

- Ps JJ Lim,2011

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 1
KUBADWA KWAYOHANE M'BATIZI
Luka 1

1. **Kodi chipangano chatsopano chisiyana bwanji ndi chipangano chakale?**
   Chipangano chatsopano chikamba za kukwaniritsa lonjezo la yesu khristu (Ahebri 1:1-2)

2. **Kodi lonjezo lake ndi loti chiani?**
   Kulumbira kwa Mulungu kuti adzapulumutsa anthu ake, ndikuwatengera kuulemerero wa kumwamba kudzera mwa Yesu Khristu. (Ahebri 6:13-20; 9:1-28)

3. **Kodi Nneneri otsiriza kulemba buku lachipangano chakale Yesu Khristu asanabadwe ndi ndani?**
   Malaki,yemwe analosera kubwera kwa Yohane M'batizi (Malakii 3:1; 4:5)

4. **Chinachitika ndi chiani mnzaka 400 za pakati pa Malaki ndikubwera kwa Ambuye Yesu?**
   Ayuda anatumikira mulungu mwa kupembeza mwa chinyengo, osati kuchokera pansi pa mtima. (Monga, Marko 1:21-22)

5. **Kodi chipembezo chinali kuyenda bwanji mnzaka 400 zimenezi**?
   Zipani zambiri za chipembezo zinayamba, monga afalisi onyenga, ndi asaduki osakhulupirira. (Mateyu 3:5-7; 12:1-14; 22:23-32)

6. **Kodi mbiri ya ndale ya Yuda mzaka zimenezi ndi yotani?**
   Kupatula nthawi yochepa,nthawi ya a Makabeo Yuda analamulidwa ndi mafuko achilendo.

7. **Kodi a Israeli onsei anatsatira Afalisi ndi Asaduki?**
   Ayi, panali mphukira zina zomwe zinapitiriza kupemphelera kubweranso kwa Mesiya. (Luka 2:25-36)

8. **Kodi analengeza kubadwa kwa Yohane mbatizi ndi ndani?**
   Mngelo Gabriel kwa Zakaliya mukachisi. (Luka 1:15-20)

9. **Kodi mngelo anaulula chiani kwa Zakaliya zokhuza Yohane.?**
   Zoti adzakhala mulosi wa ku Nazaleti, yemwe adzaitane a Israeli kuti alape. (Luka 1:15-20)

10. **Chinachitika ndi chiani kwa Zakaliya pamene sanakhulupirire za mau amene anauzidwa ndi mngelo?**
    Anakhala osamva ndi osayankhula ngati chizindikilo cha kusakhuluporira (Luka 1:20, 62-64)

Mavesi oloweza: Aroma 8:1-2

Chifukwa chache tsopano iwo akukhala mwa kristu Yesu alibe kutsutsidwa. Pakuti chilamulo cha mzimu wa moyo mwa kristu Yesu chandimasula ine ku lamulo la uchimo ndi la imfa

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2
KUBADWA KWA AMBUYE YESU
Mateyu 2 ndi Luka 2

1. **Kodi Ambuye yesu anabadwa liti?**
   Pakukwanirisidwa kwa nthawi (Agalatiya 4:4)

2. **Zitanthauzanji 'pakukwaniritsidwa kwa nthawi'?**
   Inali nthawi imene Mulungu anakonzekera zonse zofunika pakubwera kwa Mpulumutsi. (monga Gen.49:10; Daniel 9:24-26; Malaki 3:1; Marko 1:15)

3. **Ndani analengeza za kubadwa kwa Ambuye Yesu?**
   Mngelo Gabiel yemwe anamuuza Maria kuti adzakhala Mai wa Ambuye. (Luka 1:26-38)

4. **Nchifukwa chiani Yosefe ndi Maria anapita ku Betelehemu?**
   Chifukwa Kaisala Augusto analengeza kuti fuko lonse lilembedwe kalembera. (Luka 2:1-6)

5. **Kodi cholinga cha Mulungu pokonza kalembera wa Kaisala Augusto ndi chiani?**
   Kuti Yosefe ndi Maria apite ku Betelehemu mumzinda wa Davide, komwe monga mneneri Mika ananenera kuti Mpulumusi Yesu khristu adzabadwire. (Mika 5:2; Mateyu 2:5)

6. **Nchifukwa chiani Yesu anagonesedwa modyera ng'ombe?**
   Chifukwa m'zipinda zogona alendo munalibe malo. (Luka 2:7)

7. **Pali tanthauzo lililonse lauzimu pa mfundo yoti yesu anabadwira mu zodyera ng'ombe?**
   Zoona, palibe malo mu mtima mwa munthu kuti kufikira Mulungu mwini wake atapanga malowo. (Monga Yohane 19:12 -16)

8. **Ndichifukwa chiani mpulumusi anabadwira mu umphawi wotere?**
   Kuti kupyolera mu umphawi umenewu ife tikhale olemera. (2 Akorinto 8:9)

9. **Kodi mngelo anamulangiza Yosefe chiani zokhuza dzina la Mpulumusi?**
   Udzamutcha dzina lake YESU: chifukwa adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo. (Mateyu 1:21)

10. **Kodi Yesu Khristu ndi Mpulumutsi wa onse?**
    Ayi, ndi Mpulumutsi kwa okhawo osankhidwa omwe asonkhanisidwa kuchokera ku mafuko onse. (Machitidwe 2:39; onaninso Aroma 8:28-39; Aefeso 1:1-13; 2:1-22; 2 Petro 3:9; Aroma 9:6-33)

Mavesi oloweza: Aroma 8:3-4

Pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita,popeza chinafoka mwa thupi, Mulungu anatumiza Mwana wake wa Iye yekha m'chifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha uchimo, natsutsa uchimo m'thupi. Kuti choikika chache cha chilamulo chikakwaniridwe mwa ife, amene sitiyendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 3
UTUMIKI WA YOHANE M'BATIZI
Mateyu 3; Mariko 1; Luka 3; ndi Yohane 1

1. **Kodi Yohane m'batizi ndi ndani?**
   Ndi mthenga wa Ambuye. (Luka 1:76-80)

2. **Kodi ndi ulosi wanji womwe unakwaniritsidwa ndi Yohane?**
   Malaki 3:1- 'Taonani, nditumа mthenga wanga kuti akonzekeretu njira pamaso panga'

3. **Kodi ntchito ya Yohane inali yotani?**
   Anaitanidwa kuti akonzekeretse a Israel onse kubwera kwa Ambuye Yesu. (Mateyu 3:1-3)

4. **Kodi Yohane anakonzekera bwanji ntchito yake?**
   Mulungu mwini wake anamulangiza iye M'chipululu ndi kumuitanira ku ntchito yake. (Luka 1:76, 80; 3:2)

5. **N'chifukwa chiani Yohane anagwira ntchito m'chipululu?**
   Amaperekera umboni wotsutsana ndi zikhulupiriro za kayendetsedwe kokufa ka tchalitchi. (Mateyu 3:1-13; Yesaya 40:1-3; Malaki 1:6-14)

6. **Kodi Yohane amatsindika chiani mu uthenga wake?**
   Zoti anthu alape chifukwa ufumu wa Mulungu wayandikira (Mateyu 3:2)

7. **Nchifukwa chiani Yohane amalimbikira kuti ufumuwu ndi wakumwamba?**
   Chifukwa anthu amayembekeza ufumu wa dziko. (monga Yohane 6:15)

8. **Kodi Yohane anawayankha chiani akuluakulu a chiyuda amene anamufunsa kuti iye ndi ndani?**
   ' Ndine ofuwula m'chipululu .Lungamitsani njira njira ya Ambuye'. (Yohane 1:19-27)

9. **Kodi Yohane anayankha chiani pamene anthu ananena kuti iye ndi Yesu Khristu?**
   Iye anati,koma Iye wakudza pambuyo panga ali wondiposa mphamvu. Iyeyu adzakubatizani inu Ndi Mzimu Woyera ndi moto. (Mateyu 3:11; Luka 3:16; Yohane 1:33)

10. **Kodi uchimake pa utumwi wa Yohane unagona pati?**
    Anafotokozera za Ambuye Yesu kuti "ndi Mwana Wankhosa wa Mulungu amene anatenga zolakwa za anthu onse a pa dziko la pansi" (Yohane 1:29)

Vesi loloweza: Aroma 8:5

Pakuti iwo amene ali monga mwa thupi asamalira zinthu za thupi; koma iwo amene ali monga mwa Mzimu, asamalira zinthu za Mzimu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
KUBATIZIDWA KWA AMBUYE YESU NDIKUYETSEDWA KWAKE
Mateyu 3 – 4; Mariko 1; ndi Luka 3 – 4)

1. **Ndichizindikiro chanji chomwe chinayambirira pa utumiki wa Ambuye Yesu?**
   Iye anabatizidwa ndi Yohane mu mtsinje wa Yorodani. (Mateyu 3:13-17)

2. **N'chifukwa chiani Ambuye anapita kwa Yohane kuti akabatizidwe?**
   Mbali ina kuti akwaniritse kulungama kwake komanso mbali ina kuti apatulidwe ku ubatizo pa thupi lake kuti mwina tikhale ndi chinthu china chofanana naye (Calvin). (Mateyu 3:15)

3. **Kunali kofunika bwanji kwa Ambuye Yesu kuti akwaniritse kulungama konse pobatizidwa chikhalireni iye analibe tchimo?**
   Ubatizo wa Ambuyewu siunali oti uchotse machimo ake koma kuti adziyeretse yekha ku ntchito yomwe Atate wake adampatsa. (Mariko 1:4)

4. **Tingadziwe bwanji kuti uwu ndi ubatizo wa Ambuye Yesu?**
   Ansembe a chipangano cha kale amadzozedwa ndi madzi kuyeretsedwa kuutumiki akakwanitsa zaka makumi atatu ndipo Ambuye analamulira kuti Yohane agwirizane ndi maitanidwewa pomubatiza. (Luka 3:23; Numeri 4:3; 8:6-7; Luka 20:1-3)

5. **Chinachitika ndi chiani Ambuye atangobatizidwa?**
   Anatengedwa ndi Mzimu kupita ku chipululu kuti akayetsedwe ndi satana. (Mateyu 4:1)

6. **Kodi kuyetsedwa kumeneku ndikofunika bwanji?**
   Ichi ndi chiyambi cha nkhondo ya Ambuye yolimbana ndi satana

7. **Kodi satana amafuna kuti Ambuye Yesu achite chiani?**
   Amafuna kuti Ambuye asamvere Atate wake? (Mateyu 4:2-3, 6, 8-9)

8. **Chinalimbitsa mayankho a Ambuye kwa satana ndi chiani?**
   Anamuyankha satana ndi mawu a Mulungu (Mateyu 4:4,7,10)

9. **Kodi zotsatira za kuyetsedwa kwa Ambuye Yesu zimasonyeza chiani?**
   Ambuye anapambana ,ndipo adzaononga mphamvu zonse za satana ndithu. (Mateyu 4:10-11)

10. **Kodi mayesero amenewa akuphunzitsa chiani kwa ife zokhuzana ndi nkhondo yathu ndi machimo?**
    Titha kupambana m'mayesero pokhapokha kupyolera mu mawu a Mulungu ndi pemphero. (monga Luka 22:40; Masalimo 73; Chibvumb 12:10-11)

Vesi loloweza: Aroma 8:6-7

Pakuti chisamaliro cha thupi chiri imfa,koma chisamaliro cha mzimu chiri moyo ndi mtendere . Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu, pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu pakuti sichikhoza kutero.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 5
UTUMIKI WA YESU MUYUDEYA NDI MUSAMARIA
YOHANE 2 – 4

1. **Kodi chozizwa choyamba chimene Ambuye yesu anachita ndi chiani?**
   Anasandusa madzi kukhala vinyo ku Kana ku Galileya (Yohane 2:1-11)

2. **Kodi zozizwa ndi chiani?**
   Zozizwa ndi zochitika za mphamvu ya Mulungu zomwe sitingathe kudzifotokozera Mmalamulo achilengedwe.

3. **Kodi zozizwa za Ambuye zimasonyeza chiani**?
   Zimasonyeza kuti Ambuye Yesu ndi Khristu, mwana wa Mulungu. (Yohane 2:11)

4. **Ndikuti komwe Ambuye anayamba utumiki wawo m'chaka choyamba?**
   Kwenikweni ku Yudeya,komwe anagwira ntchitoyi kwa miyezi khumi. (Yohane 2:13; 3:22-23; 4:1-3; Mateyu 4:12)

5. **Kodi Ambuye Yesu anachita chiani ku Yerusalemu pamene anafika mukachisi?**
   Anathamangitsa ogulitsa ndi ogula malonda m'kachisi. (Yohane 2:13-17)

6. **Ndichizindikilo chanji chimene Ambuye Yesu anapereka kwa Ayuda kusonyeza mphamvu zake?**
   Kuwonga kachisi ndi kumumanga masiku atatu . (Yohane 2:19b)

7. **Kodi Ambuye Yesu anauza chiani Nikodemo chofunika kuchita kuti akalowe muufumu wakumwamba?**
   Abadwe mwatsopano,'Ngati munthu sabadwa mwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3)

8. **Kodi tanthauzo lenileni la mawu amene Yesu amakambirana ndi mnzimayi wa ku samaria unali wotani?**
   Ndiwoti Iye (Yesu) ndi madzi a moyo chifukwa Iye ndi Khristu. (Yohane 4:14)

9. **Kodi zotsatira za ntchito ya Ambuye Yesu kwa asamaria ndi chiani?**
   Asamaria ambiri anamukhulupilira Iye. (Yohane 4:42)

10. **Kodi chikhulupiriro cha Asamaria chimalosera chiani?**
    Chimalosera zoti Ambuye yesu adzakanidwa ndi Ayuda ndikuvomerezedwa ndi amitundu. (Yohane 4:9, 27, 35-38; Mateyu 28:19-20)

VESI LOLOWEZA: Aroma 8:8-9

Ndipo iwo amene ali m'thupi sangathe kukondweretsa Mulungu. Koma inu simuli m'thupi ai, koma mumzimu,ngatitu Mzimu wa Mulungu akhalabe mwa inu, koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu,siali wache wa Kristu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
ULENDO WOYAMBA WA AMBUYE KU GALILEYA
Mariko 2 ndi Luka 4 – 5

1. **Kodi Ambuye yesu amaphunzitsa chiani m'masunagogi a ku Nazareti?**
   Zoti iye ndiwokwaniritsa ulosi wa Yesaya wa wodzozedwa wa Mulungu. (Luka 4:16-30)

2. **Kodi anthu aku Nazareti anakhulupirira za uthengawu?**
   Ayi, zinawanyansa ndipo anafuna kumupha. (Luka 4:29)

3. **Kodi kukanidwa kwa Ambuye Yesu ku Nazareti kunapherezera chiani?**
   Anadza kwa zache za iye yekha, ndipo ache a mwini yekha sanamuandira Iye. (Yohane 1:11)

4. **Kodi Ambuye Yesu anapita kuti atachoka ku Nazareti?**
   Iye anapita ku Kaperenao,komwe anakhalitsa kwa nthawi. (Mateyu 4:13)

5. **Chinachitika ndi chiani ku Kaperenao?**
   Anachiza odwala ndi kuchotsa ziwanda. (Luka 4:40-41)

6. **Kodi Ambuye Yesu anachita chiani ku nyanja ya Galileya?**
   Anawapatsa chizindikiro chakupha nsomba modabwitsa zomwe ndipo anawaitana kuti akhale ophunzira ache ndikukhala asodzi a anthu. (Luka 5:1-11)

7. **Kodi tanthauzo la chozizwa cha kugwira nsomba zambiri ndi chiyani?**
   Kutanthauza kuti mwana wa Mulungu anasonkhanitsa mpingo wache ndi Mzimu ndi Mawu Ake. (Luka 5:10; Aroma 10:14; 2 Atesalonika 2:13-14)

8. **Ndichifukwa chiani Ambuye anachiza munthu wodwala manjenje?**
   Kudzionetsera kuti Iye mwana wa Munthu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo pa dziko lonse. (Luka 5:18-26)

9. **Afalisi ndi ndani?**
   Ndi kagulu ka Ayuda komwe kamafuna chipulumutso pogwiritsa ntchito za lamulo (Mateyu 23; Yohane 9:40 – 10:18; Mateyu 5:20)

10. **Kodi Ambuye Yesu ananena chiani kwa iwo amene amadzikhulupirira okha kuti iwowo ndi opanda tchimo?**
    Sindinabwere kudzaitana oyera mtima koma ochimwa kuti alape. (Mariko 2:17)

Mavesi oloweza : Aroma 8:10

Ndipo ngati Khristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa chifukwa cha uchimo; koma mzimu uli wamoyo chifukwa cha chilungamo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
KUTSUTSANA PA NKHANI YA SABATA NDI CHIPHUNZITSO CHA PAPHIRI
Mateyu 5 – 7: Mariko 2 ndi Yohane 5

1. **Kodi kunali kofunika kotani pa machilitso abambo wodwala ndi Ambuye pa Thamanda la Betiseba?**
   Anachilitsidwa tsiku la sabata. (Yohane 5:9)

2. **Cholinga cha Ambuye pochiza munthu tsiku la sabata ndi chiani?**
   Amafuna apeze malo onenera tanthauzo lenileni la kusunga sabata. (Yohane 5: 16-23)

3. **Kodi Ambuye anaswa sabata monga mmene Ayuda amanenera?**
   Ayi, Ambuye anasunga sabata pogwira ntchito ya Mulungu. (Yohane 5:16-23)

4. **N'chifukwa chiani Ayuda anamuda ndikutsutsana ndi Ambuye Yesu?**
   Chifukwa ananena kuti Iye ndi mwana wa Mulungu zomwe zimapangitsa kukhala ofanana ndi Mulungu. (Yohane 5:18)

5. **Kodi Ambuye anasankha ndani tsopano?**
   Anasankha ophunzira khumi ndi awiri ndipo anawatcha Atumwi. (Luka 6:12-16)

6. **Ndimalangizo otani amene Ambuye anapereka kumapeto kwa ulendo woyamba wa ku Galileya ?**
   Malangizo wokhuza ufumu wa kumwamba pa chiphunzitso cha pa phiri. (Mateyu 5 – 7)

7. **Kodi mutu weniweni wa chiphunzitso cha paphiri ndi chiani?**
   Za ufumu wa kumwamba umene wapangidwa ndi mzimu ndi mphamvu zakumwamba (monga Mateyu 5:3-20)

8. **Kodi Ambuye Yesu poyamba amanena motani pa ziphunzitso zimenezi?**
   Anafotokoza bwinobwino za mnzika zenizeni za chifumu ndi maitanidwe ao. (Mateyu 5:3-11)

9. **Kodi Ambuye akuti chiani zokhuza oyera mtima mu ufumu umenewu?**
   Ngati chilungamo chanu sichichuluka choposa cha alembi ndi Afalisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:20)

10. **Kodi maitanidwe a mnzika za kumwamba ndi wotani?**
    Muthange mwafuna Ufumu wache ndi chilungamo chache ndipo zonse zimene zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:24-34)

Mavesi oloweza: Aroma 8:11

Koma ngati mzimu wa Iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, Iye amene adaukitsa Khristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzim wache wakukhala mwa inu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
ULENDO WACHIWIRI WA AMBUYE KU GALILEYA
Luka7:19-35 ndi 8:41-56

1. **Ndi chifukwa chiani Yohane M'batizi amatumiza anthu apereke uthenga kuti amufunse Ambuye Yesu ngati analidi Khristu.?**
   Chifukwa amafuna kumva zomwe Ambuye angatsimikize ntchito yake ngati wolambula njira ya Ambuye yakwaniritsidwadi. (Mateyu 11:1-3)

2. **Kodi Ambuye anawayankha chiani otsatira Yohane?**
   Anawakumbutsa iwo za zozizwa ndi uthenga wabwino womwe Iye amalalikira umene umatsimikiza kuti ndi Iyeyo Mesia olonjezedwa. (Mateyu 11:4-5)

3. **Kodi Ambuye yesu anauza chiani unyinji wa anthu omwe sanalape atamva uthenga wa Yohane , ndipo sanalape mpaka lero?**
   Kuti adzala ndi zowilingula zokhazokha ndipo chilango chao chitha kukhala chachikulu kuposa cha Sodomu ndi Gomola. (Mateyu 11:20-24):

4. **N'chifukwa chiani ena amakhulupirira pomwe ena samakhulupirira Ambuye?**
   Chifukwa Mulungu anabisa zinthu zakumwamba kwa anzeru ndi opurikira ndipo anaululira pang'ono kwa Ana. (Mateyu 11:25-27).

5. **Kodi mafanizo ndi chiani?**
   Mafanizo ndi zinthu zooneka za dziko zomwe zimapereka tanthauzo ku zinthu za ufumu wa kumwamba. (Mateyu 13:10-17)

6. **N'chifukwa chiani mafanizo amapereka tanthauzo la zinthu za kumwamba?**
   Chifukwa Mulungu analenga dziko m'chithunzi cha zakumwamba. (monga Genesis 1:14; 49:9 Chivumbulutso 5:5; Malaki 4:2; Chivumbulutso 22:16)

7. **N'chifukwa chiani anthu onse ayenera kumvetsetsa za ufumu umenewu?**
   Kuti ochimwa onse adzasowe chowilingula ndikuti okhulupirira alimbikitsidwe m'chikhulupiriro chao. (Mateyu 13:11-15)

8. **Kodi chodabwitsa chodziwika chomwe chinangochitika nthawi imeneyi ndi chotani?**
   Ambuye yesu anaukitsa mwana wa mkazi wa Yairo. (Mateyu 9:20-26; Luka 8:41-56)

9. **Zotsatira za kuwukitsidwa kwa mwana wa Yairo zinali zotani?**
   Mbiri inamveka dziko lonse. (Mateyu 9:26)

10. **Kodi utumiki wachiwiri wa m'Galileya unathera kuti?**
    Ku Nazareti komwe Ambuye Yesu anakanidwa kachiwiri. (Mateyu 13:53-58)

Mavesi oloweza: Aroma 8:12-13

Chifukwa chache abale, ife tiri amangawa si ache a thupi ai, kukhala ndi moyo monga mwa thupi. Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi ,mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zochita zache za thupi , mudzakhala ndi moyo .

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
ULENDO WACHITATU WA AMBUYE KUGALILEYA
Mariko 6:35 mpaka mtsogolo and Yohane 6

1. **Chinachitika choyamba ndi chiani ulendo wachitatu wakugalileya?**
   Ambuye yesu anatumiza ophunzira khumi ndi awiri kwa nkhosa zotayika mnyumba za Israeli (Mateyu 10)

2. **Kodi Ambuye anauzidwa chiani nthawi imeneyi?**
   Zoti Yohane M'batizi anadulidwa mutu mundende. (Mateyu 14:3-12)

3. **Ndichodzizwa chanji chomwe Ambuye anachita atayandikira Kaperenamu?**
   Anadyetsa anthu mazana asanu kuphatikiza Amayi ndi ana ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri. (Yohane 6:1-13)

4. **Chotsatira cha chodzizwa chodyetsa anthu mazana asanu chinali chiani?**
   Anthu ochuluka anali ozizwa ndipo anamukakamiza Ambuye kuti akhale mfumu yawo ya dziko lapansi. (Yohane 6:15)

5. **Kodi Ambuye yesu anawauza chiani anthu omwe adzakhale iye mfumu yao?**
   Anawauza kuti Iye ndi mkate wa moyo ndipo ufumu wake siwadziko lapansi. (Yohane 6:30-40)

6. **Kodi aunyinji anavomereza ngati Yesu ndi mkate wa moyo?**
   Ayi, ambiri anakana ndipo anachoka. (Yohane 6:66)

7. **Kodi Ambuye anafotokozera bwanji pa mfundo yoti ambiri anamukana Iye?**
   Ananena kuti 'Kulibe mmunthu akhoza kudza kwa Ine, koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye'. (Yohane 6:44)

8. **Kodi Ambuye yesu anapita kuti atangokanidwa?**
   Anachoka ku Galileya napatukira mmalire a Turo ndi Sidoni kukachiza mwana wa mkazi wa Kanani. (Mateyu 15:21-28)

9. **Kodi Ambuye yesu anaphunzitsa chiani ophunzira ake paulendo wake wa ku Sidoni?**
   Pamene Aisraeli anakana Ambuye,Iye adzaitana anthu ake kuchokera kwa amitundu. (Mateyu 15:28; Aroma 11)

10. **Kodi kulapa kwenikweni kwa Petulo ku Kaisaliya wa Filipi kunali kotani?**
    'Inu ndinu Khristu , Mwana wa Mulungu Wamoyo', (Mateyu 16:16)

Mavesi oloweza: Aroma 8:14-16

Pakuti onse otsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu amenewo ali ana a Mulungu. Pakuti inu simunalandira mzimu wa ukapolo kuchitanso mantha; koma munalandira mzimu wa umwana , umene tinafuula nao, kuti, Abba, Atate. Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu kuti tili ana a Mulungu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
MAWALITSIDWE A YESU PA PHIRI
Mateyu 16; 18; Mariko 8 – 9; ndi Luka 9

1. **Kodi Ambuye yesu anayamba kuwauza chiani ophunzira ake Petulo atangolapa?**
   Anayamba kuwalangiza ophunzira ache za masautso ndi imfa yake. (Mateyu 16:21- 23)

2. **Kodi, molingana ndi Ambuye, ndi chiani chingasonyeze ophunzira weniweni wa Yesu?**
   Adzikane yekha, natenge mtanda wache, ndikunditsata Ambuye. (Mateyu 16:24)

3. **Chinachitika ndi chiani atatsala pang'ono kumaliza ulendo wachitatu wa Yesu ku Galileya?**
   Anasandulika pa phiri ophunzira atatu akuwona. (Mateyu 17:1-8)

4. **Ndi chifukwa chiani Mose ndi Eliya anaoneka pa phiri?**
   Chifukwa anayankhula Ambuye za imfa yawo ndi kuwuka kwawo monga mmene ananenera Aneneri ndi chilamulo. (Mateyu 17:3; Luka 9:30-31)

5. **Kusandulika kumeneku kutanthauzanji kwa Yesu?**
   Kunali kungofuna kulawa ulemerereo womwe adzalandire pakutha pa masautso ndi imfa yake. (Afilipo 2:6-11; Aheberi 1:3)

6. **Kodi cholinga cha kusandulika kwa ophunzira kunali kotani?**
   Ngati mboni zake iwo adzaperekere umboni za ulemerero wake. (2 Petulo 1:16-18)

7. **Kodi lingalilo la Ambuye Yesu pa kusandulikaku linali lotani**?
   Amakonzekera ulendo wake wopita ku Yerusalemu. (Luka 9:51)

8. **Ndichozizwa chanji chomwe Ambuye yesu anachita pa ulendo wopita ku mgonero ku Yerusalemu?**
   Anachiza a khate khumi, mmodzi anali Msamaliya yemwe anabwerera kukathokoza. (Luka 17:11-16)

9. **Kodi Ambuye Yesu anachita chiani tsiku lotsiriza la mgonero wa msunagoge?**
   Analira,'Ngati wina amva ludzu abwere kwa Ine ndikumwa" (Yohane 7:37).

10. **Kodi malingaliro Ayuda pa Yesu anali otani pa nthawi imeneyi?**
    Kangapo konse anafuna kumupha koma analephera chifukwa nthawi inali isanakwane. (Yohane 7:30; 8:20)

Mavesi oloweza: Aroma 8:17

Ndipo ngati ana, pomweponso olowa nyumba; inde olowa nyumba ache a Mulungu, ndi olowa anzache a Kristu; ngatitu ife timva zosowa pamodzi naye, kuti tikalandire ulemerero pamodzi ndi Iye.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 11
CHIUKITSO CHA LAZARO
Yohane 9 – 11

1. **Ndichozizwa chachikulu chotani chomwe Ambuye Yesu anachichita ku Yerusalemu chomwe chinapangitsa Afarisi kuyamba kumufufuza?**
   Anaukitsa munthu yemwe anabadwa wakhungu. (Yohane 9)

2. **Kodi Ambuye anadzifotokozera motani zokhuza Iye mwini mukachisi?**
   Anati Iye ndi M'busa wabwino amene amakonda nkhosa zake ndipo amadzipatsa moyo wake. (Yohane 10:1-15)

3. **N'chifukwa chiani Ayuda ochimwa sanamukhulupirire Ambuye yesu?**
   Sanamukhulupirire chifukwa iwo sanali nkhosa za pa mbuyo pake. (Yohane 10:22-31)

4. **Kodi Ambuye yesu anapita kuti pamene ayuda anafuna kumupha ku Yerusalemu?**
   Anapita ku Pereya tsidya la mtsinje wa Yorodani komwe anaphunzitsa m'zifanizo. (Yohane 10:39-42; Luka 13:22; Luka 15)

5. **Tchulani ena mwa mafanizo omwe Ambuye Yesu anaphunzitsa ku Pereya?**
   Fanizo la mwinia chuma wopusa, za nkhosa yotayika, ndalama yotayika, ndi mwana wolowerera. (Luka 15)

6. **Nchifukwa chiani Ambuye anabwerera ku Yudeya?**
   Anapita kuti akaukitse Lazaro yemwe anatha masiku anayi atamwalira. (Yohane 11:1-17)

7. **N'chifukwa chiani kuukitsidwa kwa Lazaro chinali chozizwa chachikulu kwa Ambuye?**
   Ambuye mwini anachinena ichi m'mau ake kwa Marita ' Ndine kuuka ndi moyo aliyense wokhulupirira Ine ngakhale amwalire adzakhala ndi moyo'. (Yohane 11:25)

8. **Kodi kuukitsidwa kwa Lazalo kunakhuza bwanji Ayuda?**
   Khoti lapamwamba la Ayuda linakonza chiwembu chofuna kupha Yesu. (Yohane 11:46-53)

9. **Kodi Ambuye Yesu zinawakhuza motani atamva za chiwembu cha Khoti lalikulu la Ayuda?**
   Anayamba kusayendayenda poonekera mwa Ayuda ndipo anachoka kupita ku Mzinda wa Eferemu. (Yohane 11:54)

10. **Nchifukwa chiani Yesu anawapewa Ayuda?**
    Chifukwa nthawi yake inali isanakwane (monga Yohane 2:4; 7:30; 8:20; 17:1; 18:1-3)

Mavesi oloweza: Aroma 8:18
Pakuti ndiyesa kuti masautso a nyengo yatsopano sayenera kulinganizidwa ndi ulemerero umene udzaonetsedwa kwa ife.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
KUCHOKERA KU EFEREMU KUPITA KU YERUSALEMU
Luka 18 – 20, ndi Yohane 12

1. **Tchulani ena mwa mafanizo omwe Ambuye Yesu anaphunzitsa mu Eferemu?**
   Mafanizo a oweluza a chinyengo, Afalisi ndi anthu wamba ndi antchito mmunda wa mpesa. (Luka 18:1-14; 20:9-18)

2. **Kodi Ambuye anamuyankha chiani mdindo amene anafuna moyo wosatha?**
   'Pita ndipo ukagulitse zomwe ulinazo, nupatse aumphawi, ndipo udzakhala ndi chuma kumwamba; ndipo ubwere kuno unditsate. (Mateyu 19:21)

3. **Kodi Ambuye anatsimikiza chiani zokhuza masautso ake nthawi imeneyi?**
   Ananena kuti nthawi yatsala pang'ono. (Luka 18:31-33; Yohane 12:7-8, 23, 35-36)

4. **Kodi ophunzira zidawakhuza bwanji Ambuye Yesu atawauza kuti Iye adzazunzika ndi ndikufa?**
   Sanamvetse kuti Ambuye angazunzike ndi kufa chifukwa amayembekezera kuti Iye akhale mfumu ya mdziko. (Luka 18:31-34)

5. **Ndichozizwa chanji chimene Ambuye anachita panjira ya ku Yerusalemu?**
   Anachiza Batumeyo wa khungu wa ku Yeriko. (Mariko 10:42-56; Luka 18:35-43)

6. **N'chifukwa chiani Yesu anakacheza kunyumba kwa Zakeyu?**
   Anabweretsa chipulumutso ku nyumba yake popeza iyenso anali mwana wa Abrahamu. (Luka 19:1-10)

7. **Kodi Yesu anafika liti ku Betaniya?**
   Lachisanu, patangotsala masiku asanu ndi limodzi kuti achite pasaka wotsiriza woti asanzikane ndi ophunzira ake. (Yohane 12:1)

8. **Kodi ndikunyumba ya yani komwe Ambuye Yesu ndi ophunzira anadya mgonero.?**
   Kunyumba ya Simoni wakhate komwe Maria ndi Marita pamodzi ndi Lazaro anali komweko. (Mariko 14:1-5)

9. **Kodi Maria anawonetsa bwanji chikhulupiriro chake pa mgonero wa Ambuyewu?**
   Anathira mafuta onunkhira pa thupi la Yesu monga mmene anachitira mzimayi wochimwa uja yemwe anatenga nsupa ya mafuta onunkhira ndikuzoza mapazi ake a Yesu poyambirira pa utumiki wake. (onaninso Mateyu 26:12; Luka 7:36 mpaka mtsogolo)

10. **Kodi Ambuye yesu anafotokoza bwanji za chikondi chimenechi?**
    Ananena kuti wachita izi kukonzekera kuikidwa mmanda kwake. (Mariko 14:6-9; Yohane 12:7-8)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:19-20

Pakuti chiyembekezetso cha cholengedwa chilindira bvumbulutso la ana a Mulungu. Pakuti cholengedwacho chagonjetsedwa kuutsiru chosafuna mwini, koma chifukwa cha Iye amene anachigonjetsa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
SABATA YA MASAUTSO
Mateyu 21; Mariko 11; Luka 19, ndi Yohane 13

1. **Kodi malowedwe a Ambuye Yesu mu Yelusalemu anasonyeza chizindikiro chanji cha ufumu wake?**
   Kuti ngati mfumu, Ambuye adzalowa muufumu wake ngati kapolo wofatsa. (Mateyu 21:1- 7; Luka 19:29-35; Zakar 9:9)

2. **Kodi kufunika koyeretsa kachisi kachiwiri kunali kotani?**
   Ndichizindikilo choti Ambuye anabwera kudzayeretsa mitima ya anthu onse kumachimo awo. (Luka 19:45-46; Mariko 11:16-17; Yesaya 9:6-7)

3. **Kodi linali lofunika bwanji tsiku la lachiwiri Ambuye asanapachikidwe?**
   Linali tsiku lotsiriza pa utumiki wake wa Ambuye, pomwe Iye anafotokoza zambiri za kubweranso kwake kwachiwiri, ndi chiweruzo chotsiriza. (Luka 21:5-37; onaninso Mateyu 24:4 – 25:13)

4. **Chinachitika ndi chiani pa tsiku lachitatu?**
   Ambuye yesu anawauza mawu onse ophunzira ache ndipo Yudasi anakonza chiwembu ndi akulu a Ansembe kuti ampereke Iye. (Mateyu 26:1-2, 14-16; Mariko 14:10-11; Luka 22:1-6)

5. **Kodi tanthauzo la kusuka mmapazi pa mgonero wotsiriza ndi chiani?**
   Zimatanthauza kuti Ambuye mwini anadzichepetsa ngati kapolo powasuka anthu ndi mwazi wake. (Yohane 13:2-20; Chivumbulutso 1:5-6; Afilipi 2:6-7)

6. **Ndiphunziro lanji limene Ambuye yesu anaphunzitsa ife potsuka mapazi a ophunzira ake?**
   Kuti tiyenera kutumikirana wina ndi mnzake chifukwa tasambisidwa ndi mwazi wake. (Yohane13:14)

7. **Kodi adani a Yesu anafuna kumupha Iye nthawi yomweyo?**
   Ayi, anafuna kumupha Iye mwa chinsinsi, osati tsiku la mgonero. (Mateyu 26:3-5)

8. **Kodi Ambuye yesu anawafulumiza bwanji Ayuda kuti achite mwansangasanga?**
   Anamuzuzula Yudasi kumuuza iye kuti 'Chimene uchita chita nsanga. (Yohane 13:27)

9. **Kodi Ambuye anachita chiani atamuchotsa Yudasi?**
   Anakhazikitsa sakalamenti ya mgonero wa Ambuye wotsiriza. (Mateyu 26:26-28)

10. **Kodi zizindikiro za sakalamentili ndizotani?**
    Kunyema kwa mkate ndi kuthira kwa vinyo ngati zizindikiro za kukhomedwa ndi kukhetsa mwazi.
    (1 Akorinto 11:23-26)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:21-22

Ndichiyembekezo kuti cholengedwa chomwe chidzamasulidwa ku ukapolo wa chibvundi, ndi kulowa ufulu wa ulemerero wa ana a Mulungu. Pakuti tidziwa kuti cholengedwa chonse chivuula,ndi kugwidwa m'zowawa pamodzi kufikira tsopano.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
AMBUYE YESU AGWIDWA NDI KUZENGEDWA MULANDU
Mateyu 26; Mariko 14 – 15; Luka 22 – 23; ndi Yohane 18 – 19

1. **Kodi Ambuye yesu mmunda wa Getsemani anapemphera chiani?**
   "Atate,ngati nkutheka,chikho ichi chindipirire Ine;koma si monga ndifuna Ine; koma Inu." (Mateyu 26:39)

2. **Kodi Ambuye anadzionetsera motani kuti Iye ndi wamphamvu kuposa adani ake pamene amadzamugwira?**
   Anadzidzimutsa gulu lonse lomwe linadza kudzamugwira Iye ndi mawu a mphamvu. (Yohane 18:1-12)

3. **Ndikuti kumene Ambuye yesu anamutengera koyamba atamutsekera?**
   Aninasi mpongozi wake wa Kayafa,amene anali mkulu wa ansembe chaka chimenecho. (Yohane 18:13; 19-24)

4. **Kodi bwalo lalikulu la Ayuda lomwe linazenga mlandu Yesu linaonetsa kuipa mtima kwake motani?**
   Anapeza mboni zonama zomwe zinanenera Yesu. (Mateyu 26:59)

5. **Kodi ndi malo ati kumapeto kwake pamene bwalo lalikulu la milandu linapeza kuti Iye anali olakwa?**
   Paumboni wake woti Iye ndi khristu,mwana wa Mulungu wa moyo. (Mateyu 26:63-66)

6. **Ndi chifukwa chiani zonse zimene Ambuye Yesu amamunenera kubwalo lalikulun la Ayuda zinali za boza?**
   Chifukwa zikuwonetsera poyera kuti iwo anamukana Yesu ngati Khristu. (Mateyu 26:65-68)

7. **Chinawonjezera pa masautso a Yesu pamene Iye anali kuzengedwa pamaso pa Ayuda ndi chiani?**
   Anakanidwa ndi Petulo, mmodzi mwa ophunzira odalirika. (Luka 22:54-62)

8. **Kodi maganizo a Pilato pa mlandu wa Yesu anali otani?**
   Pilato amawopa makamaka chifukwa anadziwa kuti Yesu sanalakwe. (Mateyu 27:11-25)

9. **Ndi chifukwa chiani Pilato anamuweruza Ambuye Yesu kuti aphedwe ngakhale iye anadziwa kuti Yesu sanachimwe?**
   Chifukwa iye amawopa anthu aja ndipo amafuna kulimbikitsa ubale wake ndi kaisala. (Luka 23:1-25)

10. **Kodi cholinga cha Mulungu pa kuzengedwa mulandu kwake kwa Yesu chinali chiyani?**
    Kutsimikiza kuti Yesu anangophedwa opanda cholakwa chirichonse. (Luka 23:14; 20-22; Yohane 18:28-40)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:23

Ndipo sichotero chokha, koma ife tomwe tiri nazo zoundukula za Mzimu, Inde ifenso tibuula m'kati mwathu ndi kulindirira umwana wathu,ndiwo chiomboledwe cha thupi lathu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
PAKAVARE
Mateyu 27; Mariko 15; Luka 23; Yohane 19

1. **Kodi Ambuye Yesu anafa kuti awombole anthu onse?**
   Ayi, anapereka moyo wake kwa nkhosa zomwe Atate anamupatsa Iye. (Yohane 10:11, 15, 27-29)

2. **Ndi chifukwa chiani Ambuye anafa imfa ya pamtanda?**
   Chifukwa imfa ya pantanda ndiyotembereredwa ndipo Iye anatitengera matemberero athu. (Agalatiya 3:13; Detoronomo 21:23)

3. **Kunali kofunika kotani kuti Ambuye yesu atitegere matemberero a ife kwa Yekha?**
   Kuti alipire machimo athu ndi kupeza malipiro a moyo wamuyaya. (Ahebri 9:11-22; Aroma 3:25; 5:1, 6-21)

4. **Kodi Ambuye yesu anawonetsa bwanji kuti Iye anafa imfa yokonzekekera kamba ka machimo athu?**
   Atangokhomedwa pa ntanda Iye anapemphera “Ambuye akhululukireni chifukwa sadziwa chomwe akuchita.” (Luka 23:34)

5. **Chinawonjezera masautso a Ambuye pa mtanda ndi chiani?**
   Onse amene anamuona anamulalatira ndikumunyoza. (Mateyu 27:26-31,34-44)

6. **Kodi timawerenga chiani za wochimwa awiri omwe anapachikidwa ndi Yesu pamtanda?**
   Onse awiri anamunyoza Yesu koma mmodzi analapa ndikumukumbusa Yesu kuti adzamukumbukire mu ufumu wakumwamba. (Mateyu 27:44; Luka 23:39-43)

7. **Chinachitika ndi chiani pa maola atatu a mdima?**
   Ambuye anavutika kwambiri ndi ululu wa gahena chifukwa cha machimo a anthu. (Mateyu 27:45-46)

8. **Kodi mawu oti 'kwatha' akutanthauza chiyani?**
   Kutanthauza kuti Ambuye yesu anakwaniritsa malemba ndikutsiriza ntchito imene Atate wake anampatsa kuti ayigwire. (Yohane 4:34; 17:4; Aefeso 2:14-17)

9. **Kodi Ambuye yesu anaonetsanso motani kuti ntchito yake yatha?**
   Anapereka mzimu wake mmanja mwa Atate ake amafa? (Luka 23:46)

10. **Kodi Mulungu anawonetsa bwanji kuti ntchito ya Ambuye yakwaniritsidwa?**
    Chinsalu cha mkachisi chinang’ambika pakati, dziko linagwedezeka ndipo manda a anthu ambiri oyera mtima anatseguka. (Mateyu 27:50-53)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:24-25

Pakuti ife tinapulumutsidwa ndi chiyembekezo ; koma chiyembekezo chimene chioneka si chiri chiyembekezo ayi, pakuti ayembekezera ndani chimene achipenya? Koma ngati tiyembekezera chimene sitichipenya,pomwepo tichilandira ndi chipiriro.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
KUUKA KWA AMBUYE YESU NDI KUKWERA KUMWAMBA
Mateyu 28;Mariko 16; Yohane 20 – 21: ndi Luka 24

1. **Chinachitika ndi chiani mmawa wa tsiku limene Ambuye Yesu anauka?**
   Dziko linagwedezeka ndipo mngelo anagubuduza mwalawo. (Mateyu 28:1-8)

2. **Chifukwa chiani mngelo anagubuduza mwala uja?**
   Kuti m'manda mopanda kanthu ukhale umboni kuti Yesu wauka. (Mateyu 28:5-8; Mariko 16:3-8)

3. **Kodi zofunda zake zinasonyeza bwanji kuti Ambuye wauka?**
   Atasunzumira anawona nsaru zabafuta zitakhala ngati sanalowamo. (Yohane 20:1-9)

4. **Kodi kuuka kwa Ambuye Yesu kutanthauzanji kwa ife?**
   Kusonyeza kuti anatigulira zolakwa zathu zonse ndipo anawononga mphamvu ya imfa ndi manda. (Aroma 4:25; Ahebri 2:14-15)

5. **Kodi Ambuye Yesu anatani patatha masiku makumi anayi atauka kwa akufa?**
   Anawonekera kwa ophunzira kwa kanthawi ndipo anawalangiza iwo za ufumu wa kumwamba. (monga Mateyu 28:8-10; Luka 24:13-31, 33-34; Akorinto 15:3-6; Machitidwe 1:3)

6. **Kodi cholinga cha maonekedwe a Ambuye atauka mmanda chinathandizanji?**
   Ngati umboni woti wakuuka kwake kwa akufa ndikusonyeza kuti sabata iyenera kusungidwa pa tsiku loyamba la sabata. (monga Machitidwe 1:3; Yohane 20:1-3, 10, 19; Machitidwe 20:7; 1 Akorinto 16;2; Chivumbulutso 1:10)

7. **Kodi Ambuye Yesu anachita chiani patatha masiku makumi anayi atauka m'manda?**
   Anakwera kunka kumwamba ophunzira akumuona. (Machitidwe 1:1-3; 9-11)

8. **Kodi kukwera kumwamba kwa Ambuye Yesu ndikofunika bwanji?**
   Kuti Iye anakwezedwa ndi dzanja la Atate ndipo ali ndi mphamvu kumwamba komanso padziko. (Mateyu 28:18)

9. **Kodi Ambuye Yesu akutichitira ife chiani kumwamba?**
   Akutipemphera ndikutilamulira ndi mawu ndi mzimu. (Aroma 8:34; Ahebri 9:12, 24; Aefeso 1 :20-23)

10. **Kodi Ambuye Yesu adzabwera liti?**
    Kutha kwa dziko Iye adzabweranso ndi mphamvu ndi ulemerero. (Mateyu 24:30; 25:31; Luka 9:26; Katekesimu wankulu wa Westminster F56)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:26

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti chimene tichipempha monga chiyenera sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 17
PENTEKOSITE
Machitidwe a atumwi 2

1. **Ndi chifukwa chiani buku la Machitidwe limayamba ndi kukwera kumwamba kwa Yesu?**
   Chifukwa limakamba za Ambuye wokwezedwa ndi kupitiriza kufotokoza ndi kuchita zinthu kupyolera mwa ophunzira ache. (Aefeso 4:10-14; 2 Akorinto 8:23; 12:12; Aheberi 2:3-4)

2. **Chinachitika ndi chiani pa tsiku la Pentekosite?**
   Mzimu woyera anadzadza mu Mpingo wonse. (Machitidwe 2:1,16-18; Yoweli 2:28-29)

3. **Ndi chizindikiro chanji chomwe chinatsatira kudzadzidwa kwa Mzimu Woyera?**
   Kunamveka mkokomo wa phokoso la mphepo wolimba ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana onga a moto, ndikudzazidwa onse ndi Mzimu Woyera nayamba kulankhula ndi malilime ena. (Machitidwe 2:1-4)

4. **Kodi phokoso la mphepo chinali chizindikilo chanji ?**
   Chinali chindikilo cha mphamvu ya mzimu woyera ndi ntchito yodabwitsa mmitima ya okhulupirira. (Machitidwe 2:2-4; Yohane 3:3-8)

5. **Kodi malilime ogawikana ngati a moto akutanthauzanji?**
   Mphamvu ya Mzimu Woyera kuti itsuke machimo ndikudzoza okhulupirira ku ntchito ya Mulungu. (Machitidwe 2:3; Mateyu 3:11; 1 Petulo 1:7)

6. **Kodi tanthauzo la kuyankhula ndi malilime ena litanthauza chiani?**
   Kuti uthenga tsopano ukalalikidwe ku mafuko onse. (Machitidwe 2:14-21, 39)

7. **Kodi Petulo anafotokozera bwanji zomwe zinachitika pa Pentekosite?**
   Anafotokozera zomwe anthu anali kuwona ndi kumva zinali kukwaniritsa mawu amene analosera Mneneri Yoweli. (Machitidwe 2:16)

8. **Kodi Petulo anawachenjeza chiani anthu omwe anabayidwa mmitima yawo kupyolera mu uthenga wake?**
   'Lapani,ndikubatizidwa aliyense mwa inu m'dzina la Yesu khristu kuvomereza kumachimo anu ndipo mudzalandira mzimu woyera." (Machitidwe 2:38)

9. **Kodi zipatso za umboni wa Petulo zinali zotani?**
   Anthu okwana zikwi zitatu (3000) analapa ndikubatizidwa ndipo anawonjezereka mu mpingo. (Machitidwe 2:41)

10. **Ndi mawu otonthoza otani omwe Petulo amawauza anthu?**
    Pakuti lonjezano liri kwa inu ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana. (Machitidwe 2:39)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:27
Ndipo Iye amene asanthula m'mitima adziwa chimene achisanthula Mzimu chifukwa apempherera oyera mtima monga mwa chifuniro cha Mulungu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
MAZUNZO NDI KUKULA KWA MPINGO
Machitidwe 3 – 6

1. **Kodi Ambuye anapangitsa bwanji kuti mpingo ukule mu Yerusalemu?**
   Kupyolera mu kulalikira ndi zozizwa za Atumwi. (Machitidwe 2:47b; 3:1-8; 5:40-42; ndi ena)

2. **Kodi chozizwa choyamba chotsindikizika chinali chiani?**
   Kuchilitsidwa kwa munthu opuwala opempha pa chipata cha pa tchalichi. (Machitidwe 3:1-11)

3. **Kodi kufunika kwa machilitso kwa opempha wopuwala kunali kotani?**
   Zinasonyeza kuti tsopano khristu anali chizindikilo cha ntchito ndi zodabwitsa kupyolera mwa Atumwi. (Machitidwe 5:12; Ahebri 2:4)

4. **Kodi chotsatira cha chozizwa cha machiritso a opempha opuwala chinali chiani?**
   Kupyolera mu ulaliki wa Atumwi ,anthu okwana zikwi zisanu (5000) anakhulupirira. (Machitidwe 4:4)

5. **Kodi Ayuda zinawakhuza bwanji pa chozizwa cha opuwala opempha?**
   Anakhumudwa ndi ulaliki wa Petulo ndipo anamuika Petulo ndi Yohane mu ndende. (Machitidwe 3;12 – 4:3)

6. **Kodi Petulo ndi Yohane anayankha chiani pamene anauzidwa zoti asamaphunzitse mu dzina la Ambuye yesu?**
   Pakuti sitingathe ife kuleka kulankhula zimene tinaziona ndi kuzimva. (Machitidwe 4:20)

7. **Kodi chinabweretsa mantha aakulu ku mpingo wonse ndi chiyani?**
   Imfa ya Hananiya ndi Safira chifukwa tchimo la kunamiza mzimu woyera. ((Machitidwe 5:1-11)

8. **Chinapangitsa kuti Atumwi atsekeredwe kachiwiri mundende ndi bwalo lalikulu ndi chiani?**
   Bwalo lalikulu linakwiya chifukwa Atumwi anapitiriza kulalikira ndi kuchita zodabwitsa mu dzina la Yesu Khristu. (Machitidwe 5:17-29)

9. **Kodi zotsatira za mulandu wa Atumwi kwa oweruza chinali chotani?**
   Atumwi anawakwapula ndikuwalamulira kuti asalankhule kutchula dzina la Yesu ndipo anawamasula. (Machitidwe 5:38-40)

10. **Kodi Atumwi anachilandira bwanji chizunzo chimenechi?**
    Anakondwera kuti anayesedwa oyenera kunyozedwa chifukwa cha Ambuye. (Machitidwe 5:40-42)

Mavesi a pamtima: Aroma 8:28

Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino,ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wache.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
MPINGO UFALIKIRA KUCHOKERA KU YERUSALEMU
Machitidwe 6 – 8

1. **Kodi chinachititsa ndi chiani poyambirira kuti kuzunzika kwa Mpingo kufalikire?**
   Kuphedwa kwa Stefano yemwe anali mmodzi wa madikoni woyamba. (Machitidwe 7:59 – 8:1)

2. **Chinapangitsa ndi chiani kuti Stefano amangidwe?**
   Ayuda olakika anadana ndi ulaliki wa Stefano ndipo sakadatsutsana naye. (Machitidwe 6:8-10)

3. **Ndi choyipa chotani chomwe bwalo lalikulu linamuzengera Stefano?**
   Anapeka maumboni abodza oti iye amanyoza Mulungu. (Machitidwe 6:11-15)

4. **Ndi chifukwa chiani bwalo la Ayuda linaponya miyala Stefano?**
   Chifukwa anamunamizira kuti iye ndi yemwe anampereka ndi kupha Yesu. (Machitidwe 7:51-52)

5. **Chinatsatira ndi chiani Stefano atangofa?**
   Mpingo ku Yerusalemu unazunzidwa kwambiri (Machitidwe 8:1)

6. **Kodi zotsatira za kuzunza kwa mpingo kunali kotani?**
   Wokhulupirira anabalalika kufikira ku Yudeya ndi ku Samaliya ngakhale kutali ku Antiokeya ndi Cyprus. (Machitidwe 9:1; 11:19-20)

7. **Kodi chizunzo chimechi chinapindulira chiani tchalichi?**
   Uthenga unalalikidwa paliponse ndi anthu omwe anabalalika ku maiko ena. (Machitidwe 8:4)

8. **Kodi analalikira uthenga ku Samaria ndi ndani?**
   Anali Filipo Mlaliki ana yemwe anatsatilidwa ndi Yohane ndi Petro. (Machitidwe 8:5-14)

9. **Kodi mngelo anamutumiza kuti Filipo?**
   Kwa m'dindo wa Aitiopiya yemwe anali pa ulendo wochokera ku Yerusalemu. (Machitidwe 8:26-40)

10. **Kodi zotsatira za uthenga wabwino wa Filipo kwa mndindo wa ku Aitiopiya zinali zotani?**
    Anakhulupirira ndikubatizidwa ndipo anapitiriza ulendo wake mosangalala. (Machitidwe 8:36-40)

Vesi loloweza: Aroma 8:29

Chifukwa kuti iwo amene Iye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi chifaniziro cha Mwana wache kuti Iye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
UTHENGA WABWINO KWA AMITUNDU
Machitidwe 9 – 10

1. **Kodi chipatso chimodzi mwa zipatso za mphamvu yakudzodza ya Mzimu Woyera pa Pentekosite chinali chotani?**
   Kuti uthenga ulalikidwe ku mafuko onse osati kwa Ayuda okha. (Machitidwe 2:39)

2. **Ndi zochitika zotani zomwe Ambuye anazichita pokonza njira ya uthenga wabwino kwa a mitundu?**
   Kupyolera mu kusandulika kwa Paulo, masomphenya a Petro ku Yopa ndi chipulumutso cha Koneliyasi. (Machitidwe 9:3-18; 10:8-35)

3. **Kodi Mulungu anaitana ndani kukhala mtumwi kwa a mitundu?**
   Saulo wa ku Tarisi yemwe anali mtsogoleri wozunza mpingo wa Mulungu. (Machitidwe 9:1-2, 15)

4. **Kodi Saulo anayitanidwa motani kuti akhale mtumwi**
   Yesu Khristu anamuonekera iye paulendo wake wa ku Damasiko wokazunza a Khristu. (Machitidwe 9:1-31)

5. **Kodi Paulo anakonzekera motani ngati m'mtumwi kwa a mitundu?**
   Ambuye anawululira uthenga mu chi Arabiki. (Agalatiya 1:17)

6. **Kodi chinachitika ndi chiani Saulo atasandulika mtima?**
   Chizunzo chinayima kanthawi ndipo Petro anafika kudzalimbikitsa mipingo. (Machitidwe 9:31)

7. **Kodi tanthauzo la masomphenya a zinyama zosadibwa ku Yopa ndi chiani?**
   Zimatanthauza kuti uthenga uyenera kulalikidwa kwa amitundunso. (Machitidwe 10:15, 34-35; 15:6-7)

8. **Kodi Petro anauzidwa kuti achite chiani zokhuzana ndi masomphenya a nyama zosadibwa?**
   Kuti apite kwa Koneliyo Kenturiyo wa ku Roma ku Kaisaleya kukalalikira uthenga kwa iye. (Machitidwe 10:17-35)

9. **Kodi zotsatira za uthenga wa Petro kwa Koneliyasi zinali zotani?**
   Koneliyasi ndi nyumba yake yonse anakhulupirira ndikubatizidwa. (Machitidwe 10:42-48)

10. **Kodi mpingo unamva bwanji zomwe Petro amanena za kutembenuka kwa Koneliyasi ndi nyumba yache.**
    Analemekeza Mulungu ndi kunena ,Potero Mulungu anapatsa kwa amitundunso kutembenukira mtima kumoyo. (Machitidwe 11:18)

Vesi loloweza: Aroma 8:30

Ndipo amene Iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo iwo amene Iye anawaitana; iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene Iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso ulemerero.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
PAULO NDI BARANABASI ATUMIZIDWA KUCHOKA KU ANTIOKEA
Machitidwe 11 – 13

1. **Kodi kufunika kwa mpingo ku Antiyokeya ndikotani?**
   Panali pakatikati pomwe pamachokera uthenga ndikufalitsidwa ku maiko a ku Zambwe (Asia Minor) ngakhale ku Ulaya (Europe). (Machitidwe 11:20-27; 13:1-3; ndi ena)

2. **Kodi mpingo wa kwa Antiyokeya unakhazikitsidwa bwanji?**
   Amuna a ku Kupro ndi Kurene, analalikira Uthenga Wabwino wa Ambuye Yesu kwa a Ayuda ndi Agriki. (Machitidwe 11:19-21)

3. **Kodi Mpingo wa ku Yerusalemu unaonetsa bwanji kuthandiza kwao pa ntchito ya ku Antiyokeya?**
   Anatumiza Baranaba ndipo kupyolera mu uthenga wache ambiri anabwera kwa Ambuye. (Machitidwe 11:22)

4. **Kodi Herodi anazunza motani mpingo wa ku Yerusalemu munthawi imeneyi?**
   Anapha mtumwi Yakobo ndikuika Petro mundende. (Machitidwe 12:1-3)

5. **Kodi Herodi anaphanso Petro?**
   Ayi, mngelo wa Ambuye anapulumutsa Petro ku ndende. (Machitidwe 12:4-11)

6. **Kodi chizunzo cha Herodi chinapangitsa kuti mpingo usakule?**
   Ayi, mawu a Mulungu anakula ndi kuchuluka. (Machitidwe 12:21-24)

7. **Kodi Baranaba anatenga ndani paulendo wake wa kwa Antiokeya kuti akamuthandize?**
   Baranaba anapita ku Tarisi kwa Paulo ndipo onse awiri anagwira ntchito ku Antiyokeya kwa chaka chimodzi. (Machitidwe 11:23-26)

8. **Kodi Mzimu Woyera unawauza chiani anthu a Antiyokeya?**
   "Mundipatulire Ine Banaba ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako" (Machitidwe 13:2)

9. **Kodi mpingo wa ku Antiyokeya unawonetsa chidwi pa lamuloli kutumiza Paulo ndi Banaba?**
   Inde, atatha kusala kudya ndi kupemphera anawatsanjika manja ao ndikuwatuma kuti akalalikire uthenga. (monga Machitidwe 13:3)

10. **Ndi njira yanji yomwe Paulo anatsata pa ntchito ya utumiki wake?**
    Analalikira poyamba kwa Ayuda ndipo pambuyo pake kwa a mitundu. (monga Machitidwe 13:42, 44-46; 14:1)

Vesi loloweza: Aroma 8:31-32

Ndipo tidzatani ndi zinthu izi? Ngati Mulungu ali ndi ife adzatikaniza ndani? Iye amene sanatimana Mwana wache wa Iye yekha, koma anampereka chifukwa cha ife tonse, adzalekeranji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 22
ULENDO OYAMBA WA MTUMWI PAULO KU UTUMUKI
Machitidwe 13 – 14

1. **Kodi Banaba ndi Paulo anayambirira kuti pa ntchito yao ya utumwi?**
   Kuchisumbu cha Kupro(Cyprus) kwao kwa Baranaba, ndipo anatenganso Yohane Marko. (Machitidwe 13:4-5)

2. **Kodi anatsutsa Paulo ku Pafo anali yani?**
   Baryesu, yemwe anankantha ndi khungu chifukwa anakaniza kazembe asakhulupirire uthenga. (Machitidwe 13:4-12)

3. **Kodi Paulo ndi Banaba anapita kuti atachoka ku Kupro?**
   Anapita ku Perge wa ku Pamfuliya (Asia Minor), kumene Yohane anapatukana nao. (Machitidwe 13:13)

4. **Kodi Paulo anatsindikiza chiyani mu uthenga wake kwa Ayuda aku Antiokeya wa Pisidia?**
   Zoti Yesu wowuka kwa akufa ndi chikwaniritso cha uthenga wa Chipangano Chakale. (Machitidwe 13:14-41)

5. **Kodi zotsatira za uthenga wa Paulo ndi Banaba ku Antiyokeya wa Pisidia zinali zotani?**
   Anthu ochuluka anabwera kudzamvera koma Ayuda anachita nsanje ndi kutsutsa. (Machitidwe 13:44-45)

6. **Kodi Paulo ndi Banaba anawalimbikitsa bwanji Ayuda ngakhale anatsutsidwa ndi Ayuda?**
   Ambiri anakhulupirira amene anaikidwiratu ku moyo wosatha. (Machitidwe 13:48)

7. **Kodi zotsatira za uthenga wa Paulo ndi Baranaba ku Ikoniyo zinali zotani?**
   Unali mdalitso kamba koti Ayuda ndi Ahelene anakhulupirira. (Machitidwe 14:1)

8. **Chinakakamiza Paulo ndi Banaba kuchoka ku Ikoniyo ndi chiyani?**
   Ayuda osakhulupirira anautsa mitima ya Ahelene ndikuyamba kuwazunza. (Machitidwe 14:2-7)

9. **Chinachitika ndi chiyani kwa Paulo ndi Baranaba ku Lustra ndi Derbe?**
   Poyamba anthu anayamba kuwapembeza iwo ngati milungu ndipo kenaka anawakana ndikuponya miyala Paulo. (Machitidwe 14:6-20)

10. **Kodi Paulo ndi Banaba anachita chiani paulendo wao wobwerera ku Antiokeya?**
    Anayendera mipingo yonse imene anakhadzikitsa ndikuwalimbikitsa chikhulupiriro komanso kudzoza akuluakulu pa mpingo uliwonse. (Machitidwe 14:21-23)

Vesi loloweza: Aroma 8:33-34

Ndani adzaneneza osankhidwa a Mulungu? Mulungu ndiye amene awayesa olungama; Ndani adzawatsutsa? Khristu Yesu ndiye amene adafera ,inde makamaka ndiye amene adauka kwa akufa amene akhalanso pa dzanja lamanja la Mulungu amenenso atipemphera ife.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 23
ULENDO WACHIWIRI WA MTUMWI PAULO KU UTUMUKI
Machitidwe 16 – 18

1. **Kodi Paulo anayamba bwanji utumiki pa ulendo wake wa wachiwiri?**
   Ndi Sila anayenderanso mipingo yomwe anakhazikitsa pa ulendo wake woyamba. (Machitidwe 15:36-41)

2. **Ndichifukwa chiani Paulo sanalalikire mbali zina za ku Perge wa ku Pamfulia pa ulendo wake?**
   Mzimu woyera anamuletsa ndikumulondolera ku Trowa komwe analandira masomphenya a munthu wa ku Makedoniya. (Machitidwe 16:6-10)

3. **Kodi kufunika kwa masomphenya a munthu wa ku Makedoniya ndikotani?**
   Zinatanthauza kuti Mulungu wamuyitana iye kuti akalalikire uthenga ngakhalenso ku Ulaya (Europe) kuyambira ku Filipi. (mogna Machitidwe 16:10-15)

4. **Kodi Paulo ndi Sila anazunzika bwanji ku Filipi?**
   Atangochiza msungwana wambwebwe,anamenyedwa ndikuyikidwa m'ndende. (Machitidwe 16:16-40)

5. **Kodi zotsatira zabwino za uthenga wa Paulo ku Filipi zinali zotani?**
   Mkazi wina dzina lake Lidiya wakugulitsa chibakuwa anakhulupirira ndikutembenuka mtima iye ndi a pabanja pache. (Machitidwe 16:14 mpaka kutsogoloko)

6. **Kodi zotsatira za uthenga wa Paulo ku Atesalonika zinali zotani?**
   Ahelene akupembeza ochuluka ndi mafumu kazi anakhulupirira koma Ayuda oipa anapsa nazo mtima ndipo anauza Paulo kuti achoke kupita ku Bereya. (Machitidwe 17:1-10)

7. **Kodi timawerenga zotani za anthu a ku Bereya?**
   Analandira mawu ndi kufunitsa kwa mtima wonse nasanthula m'malembo masiku onse. (Machitidwe 17:11)

8. **Kodi zotsatira za Uthenga wa Paulo ku Atene zinali zotani?**
   Anthu ambiri anamunyoza pamene anakamba za kuuka kwa akufa ndipo ochepa okha anakhulupirira. (Machitidwe 17:16-34)

9. **Kodi Paulo anapita kuti atachoka ku Atene?**
   Anapita ku Akorinto komwe Ambuye anamulimbikitsa ndi masomphenya kuti apitirize ntchito yake kumeneko. (Machitidwe 18:1-9)

10. **Kodi zotsatira za ntchito ya Paulo ku Akorinto zinali zotani?**
    Mpingo waukulu unakhazikitsidwa patatha chaka chimodzi ndi theka chiyambireni ntchito yake. (Machitidwe 18:9-11)

Vesi loloweza: Aroma 8:35-36

Adzatisiyanitsa ndani ndi chikondi cha khristu?nsautso kodi,kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza,kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsa, kapena lupanga kodi? Monganso kwalembedwa, Chifukwa cha Inu tirikuphedwa dzuwa lonse; tinayesedwa monga nkhosa zokaphedwa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 24
ULENDO WACHITATU WA MTUMWI PAULO KU UTUMUKI
Machitidwe 19 – 21

1. **Ndi m'zinda uti waukulu ku Asiya kumene Paulo anakhala nthawi pa ulendo wake wachitatu?**
   Ku Aefeso palikulu popempherera Diyana komwe anagwira ntchito kwa zaka zitatu. (Machitidwe 19:1, 8-10, 21-41)

2. **Kodi kufunika kokhala nthawi yayitali ku Aefeso kunamuthandiza chiani Paulo?**
   Paulo anapanga Aefenso malo olalikira uthenga wabwino mu mzinda onse wa Asiya. (Machitidwe 19:10)

3. **Kodi Mulungu anatsindikiza bwanji ulaliki wa Paulo ku Aefenso?**
   Mulungu anachita zamphamvu za pa zokha moti odwala anachila ndipo mizimu yonyansa inachoka ndi manja a Paulo. (Machitidwe 19:11-12)

4. **Kodi chotsatira cha ntchito ya Paulo ku Aefeso chinali chotani?**
   Mawu a Mulungu anakulirakulira ndipo anali ponseponse moti anthu ambiri akuchita za masenga anasiya ndizikhulupiriro. (Machitidwe 19:17-20)

5. **Kodi analimbana ndi Paulo ku Aefeso ndi ndani?**
   Demetriyo yemwe anali kupanga tiakachisi ta siliva ta Arteni, ndipo anadzala ndi mkwiyo nafuula kudana naye. (Machitidwe 19:23 mpaka kutsogolo)

6. **Kodi Paulo anapita kuti kuchokera ku Aefeso?**
   Anavutika kwa nthawi mu Makedoniya ndi Helene. (Machitidwe 20:1-13)

7. **Chinachitika ndi chiani ku Trowa ulendo wa Paulo wobwerera kwao?**
   Paulo anaukitsa mnyamata wakufa wotchedwa Utiko,yemwe anagwa kuchokera pa zenera pamene Paulo anali kulalikira. (Machitidwe 20:6-12)

8. **Kodi Paulo anachita chiani ali ku Mileto?**
   Anasanzikana ndi akulu onse a mu Aefenso ndipo anawayamikira iwo kuti asunge chikhulupiriro muzochita zao. (Machitidwe 20:16-30)

9. **Kodi Mzimu Woyera unamutsimikizira Paulo chiani paulendo wake wa ku Yerusalemu?**
   Unamutsimikizira Paulo kuti kumangidwa ndi kuzunzika zikudikira iye chifukwa cha Uthenga wabwino. (Machitidwe 20:23)

10. **Kodi ndi makalata ati omwe Paulo analemba m'kati mwa ulendo wake?**
    Aroma, Akorinto Woyamba, Akorinto Wachiwiri, mwinanso Agalatiya.

Vesi loloweza: Aroma 8:37
Koma m'zonsezi, Ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
PAULO AMANGIDWA NDI KUIKIDWA M'NDENDE KU ROMA
Machitidwe 23 – 28

1. **Chinachitika ndi chiani pamene Paulo anapita ku Yerusalemu?**
   Khamu la Ayuda linamugwira ndikumtulutsira kunja kwa kachisi ndipo anafuna kumupha. (Machitidwe 21:27-31)

2. **Anapulumutsa ndani Paulo ku mkwiyo umenewu?**
   Kapitao wa mkuru wa asilikali yemwe analamulira kuti amuyike mundende. (Machitidwe 21:32-34)

3. **Kodi Ambuye anamutonthoza bwanji Paulo pamene iye anatsekeredwa m'ndende?**
   Ambuye anaonekera kwa Paulo ndikumuza kuti aperekere umboni kwa anthu ku Roma. (Machitidwe 23:11)

4. **Kodi Paulo anamutengera kuti mwachinsinsi kuchokera ku Yerusalemu?**
   Ku Kaisareya komwe anamumanga kwa zaka zopitirira ziwiri. (Machitidwe 24:24-27)

5. **N'chifukwa chiani Paulo anatengedwa kupita ku Roma kumapeto kwake?**
   Chifukwa anaonekera kwa Kaisara osati kuzengedwa kawiri ku Yerusalemu. (Machitidwe 25:9-12)

6. **Chinachitika ndi chiani paulendo wa pa nyanja wa Paulo wopita ku Roma?**
   Paulo anapulumuka modabwitsa pamene sitima inachita ngozi. (Machitidwe 27)

7. **Kodi Paulo anakhala naye bwanji ku Roma?**
   Anamulola kukhala m'nyumba yake yake ndipo anali ndi ufulu olalikira Uthenga Wabwino kwa zaka ziwiri. (Machitidwe 28:16-31)

8. **Kodi Paulo amanena chiani za Uthenga pa Aroma 1:16?**
   "…Pakuti Uthenga Wabwino sundichitsa manyazi; pakuti ndi mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupirira kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene.

9. **Kodi buku la Machitidwe likutsindika zimene tikuwerenga pa Aroma 1:16?**
   Zoonadi, chifukwa mpingo waung'ono wa khristu unakulakula kuchokera ku Yerusalemu kukafika ku Roma.

10. **Kodi chinamulimbitsa mtima ndi chiani Paulo atakumana ndi imfa?**
    "Ndalimbana nako kulimbana kwabwino ,ndatsiriza njirayo, ndasunga chikhulupiriro;chotsalira wandiikira ine korona wa chilungamo ,amene Ambuye , woweruza wolungama,adzandipatsa ine tsiku lijalo ; ndipo sikwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ache. (2 Timoteyo 4:7-8).

Mavesi oloweza: Aroma 8:38-39

Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa,ngakhale moyo,ngakhale angelo,ngakhale maufumu,ngakhale zinthu zilipo,ngakhale zinthu zirinkudza,ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chiri chonse, sichingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu, chimene chiri mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media